

BUMBA EDUCATION ZONE PRIMARY EXAMINATIONS



2025 - 2026 STANDARD 8 ZONAL MOCK

CHICHEWA (100 malikisi)

Lachiwiri, 03rd March, 2026

NTHAWI: 2hrs 15 mins

1:00pm – 3:15pm

DZINA LA OPHUNZIRA: SEX:

SUKULU: ZONI:

MALANGIZO

- Pepala ili lili ndi magawo anayi; A, B, C ndi D
- Lembani dzina lanu pamwamba pa tsamba lililonse

GAWO A (MALIKISI 30)

Yankhani funso **limodzi** lokha mwa mafunso awiri ali m'munsiwa. Mawu a chimangirizo kapena kalata asachepere 100 koma asabzole 150.

1. Lembani chimangirizo pa mutu wa, **'MASEWERA A KUMUDZI KWATHU.**

Mwazina, tsatani izi polemba:

Ndime yoyamba

- Dzina la masewera omwe amachitika kwanu
- Komwe masewerawo amachitikira
- Nyengo yomwe masewerawo amachitikira

Ndime yachiwiri

- Zinthu zomwe amagwiritsa ntchito pa masewerawo
- Kufunika kwa masewerawo
- Magulu a anthu omwe amachita masewerawo

Ndime yachitatu

- Zomwe anthu akumudzi kwanu akuchita kuti masewerawo asaiwalike

KAPENA

2. Lembani kalata kwa makolo anu omwe akukhala kunja kwa dziko lino yowapempha ndalama zolipilira ulendo womwe sukulu yanu yakonza wokaona nyama ku nkhalango ya boma

Mwazina, tsatani izi polemba.

Ndime yoyamba

- Dzina la nkhalango komwe mudzapite
- Tsiku lomwe mudzapite
- Ndalama zomwe zikufunika

Ndime yachiwiri

- Zomwe mukuyembekezera kukawona
- Kufunika kwa ulendowo

Ndime yachitatu

- Chisangalalo chomwe mudzakhale nacho mukadzapita nawo ku ulendowo

[illegible]

3. Werengani nkhani yotsatirayi mosamala kenaka yankhani mafunso otsatirawa

Nyadani adali mtsikana wokongola
kwambiri pa sukulu ya Bolero. Kwawo kwa
Nyadani kudali ku Kaswadongo. Makalo
ake adali anthu oopa Mulungu ndipo
adayesetsa kulangiza ana awo onse za
moyo wa uzimu. M'mimba ndi m'chipala,
Nyadani adapatuka ndithu. Nyadani adali
wamwano komanso okonda chiwerewere.
Ngakhale izi zidali choncho, makolo ake

Mwadzidzidzi tili m'kalasi tidawona mayi
Ndalapa akulowa m'kalasi. Adagwira khosi
la Nyadani ndikumung'ambira zovala.

“Unene komwe kuli abambo a Tito.”
Adakalipa Nasimango. “zoona ndizidya kholowa tsiku ndi tsiku pamene amuna anga ndalama akuthera iwe?” tidaonera ndewu ya mtima bii. Zinali za manyazi kumuwona Nyadani ali bunobwamuswe. Nyadani adasiya sukulu chifukwa cha manyazi.

Mafunso

a) Tchulani dzina la yemwe adamangira chitenje pamimba. (Malikisi 1)

b) Kodi makolo ake a Nasimango adali yani? (Malikisi 2)

c) N'chifukwa chiyani Nyadani adapezeka maliseche? (Malikisi 2)

d) Tchulani makhalidwe **awiri** a Nyadani. (Malikisi 2)

e) Ndi zinthu **ziwiri** ziti zomwe Nyadani amapatsidwa ndi makolo ake? (Malikisi 2)

f) Fotokozani chifukwa chimene Nyadani adasiyira kulowa m'kalasi. (Malikisi 2)

g) Pezani zining'a m'nkhaniyi zomwe matanthauzo ake ndi awa:

i. wamaliseche

_____ (Malikisi 1)

ii. wolempera

_____ (Malikisi 1)

iii. kutulukira mwadzidzidzi

_____ (Malikisi 1)

h) Tchulani dzina la mwana wa mayi ndi bambo Ndalapa. (Malikisi 1)

i) Perekani mawu ofanana m'matanthauzo ndi awa:

i. Chigwada (Malikisi 1)

ii. Kholowa (Malikisi 1)

iii. Mwano (Malikisi 1)

j) Mwaphunziramo chiyani m'mkhaniyi? (Malikisi 2)

GAWO C (MALIKISI 10)

Yankhani mafunso onse awiri m'gawoli

4. a. Werengani kankhanika ndipo muyankhe mafunso otsatirawa:

“Chaka chino ndaganiza mozama. Ndikufuna kuti tonse fibzale mbewu yamakono ya chimanga kuti m'mudzi muno musadutsenso galu wakuda.”

Mafunso

i. Ndi malonje anji amenewa?

_____ (Malikisi 1)

ii. Kodi malonjewa akuyankhulidwa kwa yani?

_____ (Malikisi 1)

iii. Mawu oti 'galu wakuda' akutanthauzanji?

_____ (Malikisi 1)

b. Lembani udindo wa munthu yemwe amathandizira mfumu.

_____ (Malikisi 2)

c. Tchulani ubwino wopita kukayezetsa magari m'zimayi akakhala woyembekezera. (Malikisi 1)

KUPANGA ZIGANIZO

5. Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa:

a) wamfupi

b) mu

c) mayo!

d) msanga

e) mwina

GAWO D (MALIKISI 40)

Yankhani mafunso onse a m'gawoli pozunguliza A, B, C kapena D

Mafunso 6 mpaka 10. Sankhani mitundu ya mawu omwe atsekedwa mzere kunsiku kwawo m'ziganizo zotsatirazi

6. "Chete!" anatero wapampando.

- | | |
|------------|--------------|
| A. mfuwu | C. mnene |
| B. mvekero | D. mfotokozi |

7. Uyu sanadye nawo.

- | | |
|----------------|--------------|
| A. mlowam'malo | C. mperekezi |
| B. dzina | D. mfotokozi |

8. Yusufu adagwa pansu kuti khu.

- | | |
|--------------|------------|
| A. mperekezi | C. mfuwu |
| B. muonjezi | D. mvekero |

9. Mwana waulemu amamvera makolo.

- | | |
|--------------|--------------|
| A. dzina | C. mlumikizi |
| B. mfotokozi | D. muonjezi |

10. Tiende mofulumira zedi.

- | | |
|-------------|--------------|
| A. mnene | C. mfotokozi |
| B. muonjezi | D. mvekero |

Mafunso 11 mpaka 15. Sankhani mitundu ya nsinjiro za chiyankhulo zotsatirazi.

11. Chidziwe umo, mlamba ndi umodzi.

- | | |
|---------------|----------------|
| A. ntchedzero | C. nseketso |
| B. ndagi | D. chifanifani |

12. Kuning'a pamimba ngati mavu.

- | | |
|----------------|---------------|
| A. chinin'ga | C. mkuluwiko |
| B. mzimbayitso | D. ntchedzero |

13. Kodi mbuzi m'kasaka zimalowa?

- | | |
|---------------|----------------|
| A. ntchedzero | C. nseketso |
| B. ndagi | D. chifanifani |

14. Wayabwidwa ndi chitedze.

- | | |
|--------------|---------------|
| A. ndagi | C. ntchedzero |
| B. chining'a | D. mkuluwiko |

15. Watchera kumwezi nkhangazaona.

- A. ntchedzero C. chining'a
- B. mzimbayitso D. mkuluwiko

Mafunso 16 mpaka 20. Sankhani magulu a mayina omwe atsekedwa mzere kungsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi

16. Kalata yanga ndalandira lero.

- A. Ka-, Ti- C. I-, Zi-
- B. Chi-, Zi- D. U-, Ma-

17. Aphunzitsi amakonda kuwerenga.

- A. Ku-, Pa-, Mu-
- B. I-, Zi-
- C. Chi-, Zi-
- D. Ku+ tsinde la mneni

18. Maulalo ndi ofunika.

- A. U-, Ma- C. Li-, Ma-
- B. Ka-, Ti- D. Chi-, Zi-

19. Mkango wagwira mbuzi.

- A. Li-, Ma- C. Mu-, Mi-
- B. Mu-, A- D. U-, Ma-

20. Ndege yafika nthawi yabwino.

- A. U-, Ma- C. Chi-, Zi-
- B. I-, Zi- D. Mu-, Mi-

Mafunso 21 mpaka 25. Sankhani mitundu ya nthambi yomwe ili ndi mzere kungsi kwake m'ziganizo zotsatirazi

21. Nkhuku imene ikudwala ndi yanga.

- A. yamfotokozi C. yoima payokha
- B. ya dzina D. ya muonjezi

22. Aphunzitsi adanena kuti tiwerenge.

- A. ya mfotokozi C. ya muonjezi
- B. ya dzina D. yoima payokha

23. Tipita tonse kumene amayi anatituma.

- A. ya dzina C. ya muonjezi
- B. ya mfotokozi D. yoima payokha

24. Agogo adafuula pamene adaona kambuku.

- A. ya dzina C. ya muonjezi
- B. yoima payokha D. ya mfotokozi

25. Zonse zikusonyeza kuti munthuyo anali wakuba.

- A. ya muonjezi C. ya mfotokozi
- B. ya dzina D. yoima payokha

Mafunso 26 mpaka 28. Sankhani mikuluwiko yomwe ikutsutsana m'matanthauzo ndi yomwe mwapatsidwa

26. Ukayendera mzengo usamati asakwi afumbula.

- A. Pakadafunda padajiwitsa galu
- B. Ukayenda m'tchire wayendera zonse
- C. Zengerezu adalinda kwawukwawu
- D. Ichi n'chiyani nkulinga muli awiri

27. Mwana wamnzako ndi wako yemwe ukachenjera manja umadya naye.

- A. Mutu umodzi susenza denga
- B. Fodya wako ndi uyo ali pamphuno

C. Mwana wamwini ndi gaga saundika

D. Ali dere n'kulinga utayenda naye

28. Kuona maso a nkono n'kudekha.

- A. Zengerezu adalinda kwawo kwawo
- B. Fodya wako ndi uyo ali pamphuno, wapachala ngwamphepo
- C. Pakadafunda padajiwitsa galu
- D. Pawiripawiri sipauzirika

Mafunso 29 ndi 30. Sankhani kanenedwe ka aneni kaziganizo zotsatirazi

29. Kodi mukulemba mayeso?

- A. Kolamula C. Kopempha
- B. Kofotokoza D. Kachifundo

30. Nyamuka msanga uzipita.

- A. Kofotokoza C. Kolamula
- B. Kachifundo D. Kopempha

Mafunso 31 mpaka 35. Sankhani mitundu ya aonjezi omwe ali ndi mzere kungsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi:

31. Iye amavina mothimbwizika.

- A. Wa malo
- B. Wa nthawi
- C. Wa mchitidwe
- D. Wa chiwerengero

32. Mtsikana abwera mawa.

- A. Wa mchitidwe
- B. Wa malo
- C. Wa nthawi
- D. Wa chiwerengero

33. Ndagogoda kwambiri koma sanandiyankhe.

- A. Wa nthawi
- B. Wa mchitidwe
- C. Wa muyeso
- D. Wa chiwerengero

34. Katundu yense adagwa pansi.

- A. Wa mhitidwe
- B. Wa malo
- C. Wa muyeso
- D. Wa nthawi

35. Watenga awiri okha.

- A. Wa malo
- B. Wa mchitidwe
- C. Wa nthawi
- D. Wa chiwerengero

Mafunso 36 ndi 37. Sankhani chiganizo chomwe chili ndi zizindikiro zam'kalembedwe zoyenera m'ziganizo zotsatirazi:

36.

- A. Zoona iyeyu adanena zimenezi.
- B. Zoona, iyeyu adanena zimenezi.
- C. Zoona iyeyu, adanena zimenezi.
- D. Zoona iyeyu adanena, zimenezi.

37.

- A. Kalanga ine! Ndiwo zija zapserera.
- B. Kalanga ine. Ndiwo zija zapserera.
- C. Kalanga ine, ndiwo zija zapserera.
- D. Kalanga ine ndiwo zija zapserera.

Mafunso 38 mpaka 40. Sankhani msintho wa aneni omwe uli ndi mzere kungsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

38. Masula mabataniwo.

- A. wochitirana
- B. wochititsa
- C. wom'chitira
- D. wotsutsana

39. Agogo awaphikira chinangwa.

- A. wochititsa
- B. wochitirana
- C. wom'chitira
- D. wochitidwa

40. Mlonda wanga wabetsa katundu.

- A. wochititsa
- B. wochitidwa
- C. wochititsa
- D. wom'chitira

Mafunso 41 ndi 42. Sankhani ntchito za 'ndi' yemwe ali ndi mzere kungsi kwake m'ziganizo zotsatirazi

41. Mtolo wa nzimbe uli ndi.

- A. mperekezi
- B. mlumikizi
- C. mvekero
- D. mlowam'malo

42. Ndidzalembe mayeso chaka chamawa.

- A. mlowam'alo
- B. mvekero
- C. mperekezi
- D. mnene

Mafunso 43 mpaka 45. Sankhani mitundu ya alumikizi omwe atsekedwa mzere kungsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

43. Amalume andipatsa malaya ndi nsapato.

- A. Wa mnene
- B. Wa dzina
- C. Wa mfotokozi
- D. Wa muonjezi

44. A Bengo anabwera ndipo apita.

- A. Wa mfotokozi
- B. Wa dzina
- C. Wa muonjezi
- D. Wa mnene

45. Mwana wanga akugwira ntchito mwamphamvu ndi mwaluso.

- A. Wa mfotokozi
- B. Wa dzina
- C. Wa muonjezi
- D. Wa mnene

MAFUNSO ATHERA APA!